Mailbox Club ikupasilani




# MULUNGU ali ngati ndani?

**Gawo La Chiwiri**

**Wokondeka mnzanga,**
Kodi unayamba waganizako kuti Mulungu ali ngati ndani? Mulungu ndi wamkulu ndi wodabwitsa kwambiri, mwakuti sitingathe kudziwa zonse zokhudza Iyeyo. Koma Mulungu watipatsa buku lodabwitsa lomwe limatiuza zambiri za iye.

**Buku limeneli ndi liti?** Ndi Baibulo, limene liri Mau a Mulungu. Baibulo limatiuza kuti Mulungu analenga zinthu zonse. Mulungu analenga dzuwa ndi mwezi. Analenganso nyenyezi zambiri mbiri zomwe zimawala usiku mu mlengalenga. Mulungu anapanganso ife anthu. Inalengedwa kuti tidzimukonda Mulungu ndiponso kuti Iye adzitikonda.

**Mulungu amadziwa ndipo amakonda** wina aliyense wa ife. Pamene ukonda winawake, umafunanso kuti iyeyo akukonde.

**Zimamukondweresa Mulungu kwambiri** pamene tifunitsita kumudziwa komanso kumukonda. Kumudziwa ndikumukonda Mulungu ndi chinthu chabwino kwambiri kuchichita. Zidzatipangitsa kukhala wokondwa.

Mu phunziro ili tiwona zomwe Baibulo limatiuza. Tiphunzira zinthu zisanu zokhudzana ndi kudabwitsa kwa Mulungu wathu yemwe amatikonda kwambiri.



## MULUNGU *ndi wamkphamvu zonze*

**Izi zikutanthauza** kuti Mulungu ali ndi mphamvu zonse kumwamba ndi dziko lapansi.Angathe kuchita china chilichonse. Palibe chosatheka ndi Mulungu. Baibulo limanena kuti, “Pajatu palibe kanthu kosatheka ndi Mulungu.” (Luka 1:37).

**Mulungu ali ndi mphamvu ZONSE.** Mafumu onse ndi atsogoleri onse amaiko m’dziko lapansi sali kanthu konse tikawafananiza ndi Mulungu. Chifukwa choti ali ndi mphamvu zonse, Mulungu angachite chilichonse wafuna kuchichita.

## MULUNGU *ndi Mzimu*

**Kodi mumadabwa** chifukwa chomwe simumuona. Mulungu ndi Mzimu konsekonse. Iye alibe thupi monga mmene ifeyo tiliri. Ndi chifukwa chake sitingathe kumuona.

Baibulo limanena kuti,**“Mulungu ndi mzimu,** ndipo ompembedza Iye ayenera kumpembedza mwauzimu ndi moona.” (Yohane 4:24)

**Ngakhale sitingathe kumuona Mulungu,** tikhoza kumudziwa ndipo tikhoza kumukonda. Pamene tamudziwa, tidzamukonda ndipo tidzamukhulupirira.

## MULUNGU *ndi waulemerero*

**Ulemerero wa Mulungu ndi wowala** kwambiri mwakuti sitingathe kumuona. Sitingathe kuliyang’ana dzuwa pamene likuwala kwambiri. Limatithobwa m’maso. Titati tiliyang’ane kwa nthawi yayitali, tikhoza kukhala akhungu. **Ulemerero wa Mulungu ndi ndi wowala koposa dzuwa.** Ichi nchifukwa chake sitingathe kumuyang’ana Iye. Mulungu anati,“…chifukwa palibe munthu angathe kundiwona Ine, nakhala moyo.”(Eksodo 33:20)

Baibulo limanena za munthu wina dzina lake Mose. Mose anali bwenzi lapamtima la Mulungu. Iye amalankhula ndi Mulungu, ndipo Mulungu amalankhula naye nthawi zambiri. Koma Mose sanamuone Mulungu Tsiku lina Mose anapempha Mulungu kuti amukomere mtima mwapadera. Iye anati,“Chonde mundiwonetse ulemerero wanu.”(Eksodo 33:18)
Mulungu anati kwa Mose,“Koma sungathe kuwona nkhope yanga,



chifukwa palibe munthu angathe kundiwona Ine, nakhala moyo.” Adapitirira
kunenanso kuti,“Pafupi ndi Ine pano pali thanthwe, iwe uimirire pathanthwepo. wanga ukamapita, ndikuika mu mng'alu wathanthwe, ndipo ndikuphimba ndi dzanja langa mpaka nditabzola.”


**Mose anakwera** kuphiri ali yekha. Mulungu anamubisa pakati pa ma nthathwe. Kenaka Mulungu analola kuti ulemerero wake udutse pamene panali Mose. Mose sadamuone Mulungu, koma anaonako pang’ono ulemerero wa Mulungu, ndipo Iye anapangitsa nkhope yake ya Mose kuti iwale monga dzuwa.
**Pamene Mose anatsika** kuchokera m’phiri lija, nkhope yake inali yowala kwambiri mwakuti anthu ankamuopa. Moti sizodabwitsa kuti Mose ndi anthu onse anati, “Inu Chauta, kodi pali Mulungu wina wofanafana nanu? … amene muli aulemu chifukwa cha ungwiro wanu?” (Eksodo 15:11)

## MULUNGU *ndi WOYERA*

**Izi zikutanthauza kuti Mulungu ndi woyera** ndi wangwiro ndipo alibe uchimo wina uliwonse. Mu Baibulo nthawi zina mdima umayimira uchimo. Baibulo limanena za Mulungu kuti: “Mulungu ndiye kuwala, ndipo mwa Iye mulibe mdima konse.” (1 Yohane 1:5)

**Mulungu ndiye kuwala ndi ulemerero wokhawokha.** Mulungu ndiwa chiyero. Mulungu sachimwa. Nthawi zonse Mulungu amachita zimene zili zabwino ndi zolondola. Palibe chilichonse chokhudzana ndi uchimo chimene chingafike pamaso pa Mulungu. Baibulo limanena kuti, “Chauta, Mulungu wathu, ndi woyera.” (Masalimo 99:9)

**Tsiku lina Mulungu adalankhula kwamneneri**Adalankhula naye m'masomphenya.Masomphenya amakhala ngati maloto.M'masomphenya ake, iye adaona Mulunguali pa mpando wake wachifumu.Pozungulira mpandowo panali angelookhaokha, amene amalemekeza Mulungundi kumanena kuti,"Ngwoyera, ngwoyera, ngwoyera Chauta Wamphamvu zonse, ulemererowake wadzaza dziko lonse lapansi." (Yesaya 6:3)
**Pamene Yesaya adawona masomphenya a Mulunguwo,**iye adachitamantha. Masomphenyawo anamuonetsa kuti iye anali munthu wochimwa ndikuti Mulungu ndi woyera.




**MULUNGU** *Ndiye Chikondi*

**Izi zikutanthauza**kuti Mulungu amatikonda ndipo Amatifunira zabwino zonse.
**Kodi timadziwa bwanji kuti Mulungu amatikonda?**Timadziwiraizi m'njira ziwiri:
• Timadziwa chifukwa chakuti Iye adanena choncho. M'mau akeMulungu amanena kuti, "ndakukondani kwambiri ndi chikondi chopanda malire," (Yeremiya 31:3)
•Timadziwanso chifukwa Iye anatumiza Mwana wake wobadwa yekhakudzatifera.

**Mukhoza kumaganiza kuti**, "Kodi Mulungu amadziwa zonsezokhudza zoipa zimene ndinanena ndi kuchita." Inde, Mulungu amadziwa zonse zokhudza machimowo, komabe amakukonda ndi mtima wakewonse. Iye amakukonda mphindi iliyonse ya moyo wako.

**Mulungu anaonetsa chikondi chake kwa ife**wake, Ambuye Yesu, kuti adzafe chifukwa cha machimo athu. – koman-so zoipa zimene ifeyo tidachita. Baibulo limanena kuti, "KomaMulungu adatsimikiza kuti amatikonda kwambiri,chifukwa pamene tinali ochimwabe, Khristu adatifera." (Aroma 5:8).

**Ambuye Yesu anafa pa mtanda chifukwa cha machimo AKO.** Koma sanakhale m'manda kwa masiku ambiri. Iye anauka kuchokeram'manda pa tsiku lachitatu. Iye ndi Mpulumutsi wathu wamoyo.Mulungu akufuna kuti iweyo umukhulupirire Iye monga ameneadakufera machimo ako ndi kuukanso kwa akufa kuti adzakhaleMpulumutsi wako.

**Kodi ukudziwa kuti Mulungu akufuna** pafupifupi zonse kuchokera kwa iwe? Iye amafuna chikondi chako! Iye akufuna iweyo kuti udzimukonda Iye ndi mtimawako wonse.


**Zimamukondweretsa Mulungu** pamene iweyo usankha kumukonda Iye ndimtima wako wonse. Mfumu Davide ndi mmodzi mwa anthu akuluakulu odziwika bwino m'Baibulo. Iye anasankha kukonda Mulungu. Iye ananena kuti,"Ndidzakukondani, inu Chauta!" Izi zinamusangalatsa Mulungu, ndipo ngati musankha kumukonda iye monga adachitira Davide, zidzamusangalatsa kwambiri. Pemphero ili ndi loti likuthandizeni:


**"Wokondeka Mulungu, ineyo ndikufuna kukukondani ndi mtima wangawonse. Chonde ndithandizeni kudziwa zambiri za Inu. Zikomo chifukwa choti mumandikonda ndi kuti mudatumiza Mwana Wanu, Ambuye Yesu, kuti adzafe chifukwa cha machimo anga."**







Ngwiritsani ntchito kiyi wachinsinsi kupeza yakho lolondola



## *Chuma chopezeka!*





**"KODI NDINGACHITE CHIYANI KUTI NDIKHALE MWANA WA MULUNGU?"**

**A.**- Uvomereze kuti ndiwe munthu wochimwa.

**B.**– Khulupirira kuti Yesu ndiye amene anafa chifukwa cha machimo ako.

**C.**– Ufike kwa Yesu ndipo umulandire Iye kukhala Mpulumutsi wako.

"Ambuye Yesu, Ine ndikumva chisoni kwambiri chifukwa cha Machimo anga. Ndikukhulupirira kuti nu ndinu Mwana wa Mulungu ndi kuti munafa pamtanda chifukwa cha machimo anga. Panopa ndikukulandirani kuti mulowe mumtima mwanga kukhala Mpulumutsi wanga." (Yohane 1:12)

# TSAMBA LA MAFUNSO
# AKALONDOLONDO 1 - PHUNZIRO 1

**MALANGIZO:** Sankhani yankho lolondola – a kapena b.
Yankho lanulo mulilembe mukabokosi kali kumanzereku.

**Chitsanzo: Kumwamba ndi malo amene**

[ b ] a.kuli uchimo wochepa.
b.kulibe uchimo.

**1.Baibulo likamanena kuti Mulungu ndi wamphamvu zonse, likutanthauza kuti**

[ ] a.Mulungu ali ndi mphamvu zambiri Kumwamba ndi padziko lapansi.
b.Mulungu ali ndi mphamvu zonse Kumwamba ndi padziko lapansi.

MULUNGU
Ndi wamphamvu zonse

**2. Sitingathe kumuona Mulungu chifukwa**

[ ] a.Mulungu ndi mzimu ndipo sitingathe kuona mzimu.
b.Mulungu ali kutali kwambiri mwakuti sitingathe kumuona.

**3.Pamene Baibulo likunena kuti Mulungu ndi woyera, likutanthauza kuti**

[ ] a.Mulungu ndi wabwino kwambiri.
b.Mulungu wopanda banga ndiwangwiro ndipo alibe tchimo lina lililonse.

MULUNGU
ndi Mzimu

**4.Timadziwa kuti Mulungu amatikonda chifukwa**

[ ] a.Iye anatipatsa Mwana Wake kuti adzafere machimo athu
b.Ife timamva monga mmene amamvera Iyeyo.

MULUNGU
ndi WOYERA

**5.Chimene Mulungu amafuna kwa ife koposa zonse ndi**

[ ] a.Chikondi chathu.
b.Kuti ifeyo tidzichita zinthu zabwino.

MULUNGU
ndi Chikondi

Lembani vesi yanu
yapamtima apa:

*Lemban apa chumachopezeka!*



Dzina ______________________________ Tsiku lobadwa ___/___/___ Zaka ____
Malo amene mumakhala __________________________________________________

# Ulendo wanga ndi Yesu!

1. Kodi chithu chofunika chomwe mwa phunzira pa phunziro limeneli ndi chiyani?

2. Kodi pali china chomwe simunamvetse mu phunziro limeneli?

3. Kodi muli ndi chosowa kapena pephero loku ti tikuthandizeni kupephera?

4. Tikukulimbikitsani kuti muyambe kulemba magazini. Lembani mapemphero anu, matamando ndi chiyamiko kwa Mulungu!